



IUF : UNITING FOOD, FARM & HOTEL WORKERS WORLDWIDE

8 RAMPE DU PONT-ROUGE | 1213 PETIT-LANCY | SWITZERLAND | IUF@IUF.ORG

## IUF COVID-19 ZOFUNA: ZAULIMI

Mliri wa COVID-19 waonetsa kufooka pa ndondomeko zathu za zakudya zomwe kwambiri zaoneka pa kusowa kwa ntchito zabwino kwa anthu ambiri omwe amagwira ntchito zaulimi. Kutseka kwa malo olova ndi kutulukira maiko komanso komanso njira zadzidzidzi zothana ndi mlirifu kwaika chiopsezo kapezedwe ka ndalama komanso umoyo wa ogwira ntchito zaulimi, umoyo wawo komanso chitetezo chawo ndi maanja awo. Ogwira ntchito mminda ndi malo ena monga nkhalando ali pachiopezo chosaikidwa pa ndondomezo zofunika chisamaliro komanso chotetezeka umoyo wawo.

Ogwira ntchito omwe ndi mzika za maiko ena ali pachiopezo chachikulu. Migwirizano ya ogwira ntchito amaletsa kapenanso kuipondeleza; ogwira ntchito za ulimi ochepa ndamene ali otetezeka ndi migwirizano yokhazikika. Ogwira ntchito 5 pa 100 aliwonse okha mu ntchito za ulimi ali ndi kuthekela kounikiridwa magwiridwe awo a ntchito kapena kutetezeka ndi malamulo zokhudza umoyo wawo komanso ufulu wawo okhala otetezeka.

Bungwe la United Nations' International Labour Organization (ILO) yakonza ndondomeko za maiko onse (onani pansipa) zoteteza ufulu, umoyo ndi chitetezo cha ogwira ntchito zaulimi. Ichi chikupeleka ndandanda wa zomwe migwirizano ya ogwira ntchito za ulimi ikufuna poteteza ogwira ntchito mza ulimi.



**CHIFUKWA OGWIRA NTCHITO ZA ULIMI NDI OFUNIKA PA CHISAMALIRO CHA CHAKUDYA, IUF IKUPEMPHA MAIKO, OLEMBA ANTHU NTCHITO NDI MABUNGWE A MMAIKO ENA KUTI AKHAZIKITSE NJIRAZI POTETEZA OGWIRA NTCHITO ZA ULIMI NDI MAANJA AWO.**

Olemba anthu ntchito apeleke malo okhala omwe akhale ndi:

- Madzi okwanira abwino, zipangizo zaukhondo ndi ofolela bwino.
- Kugona, kudya ndi zipangizo zaukhondo zilemekeze kufunika kopasana mpata waukulu bwino.
- Sopo, madzi abwino, zophela tizilombo komanso zipangizo zina zofunikira paukhondo zidzipezeka nthawi zonse komanso mogwirizana ndi ndondomeko zovomelezeka pa dziko lonse zothanirana ndi kufala akwa mliri wa COVID-19.
- Uthenga okhudza ukhondo ndi chisamaliro ukuyenera kukhala ofunikira komanso opezeka mziyankhulo zonse zomwe ogwira ntchito amagwiritsa ntchito.
- Njira zolumikizirana monga nambala zopelekera uthenga wa dzidzidzi zikuyenera kupezeka nthawi zonse.

Mwai olandira chithandizo cha mankhwala

- Ogwira ntchito onse komanso am'banja mwawo, kuphatikizapo ogwira ntchito moyendera nyengo, mzika za maiko ena komanso posayendera mmene akukhalira mdzikomo, akuyenera kukhala ndi mwayi olandira zipangizo zaumoyo komanso chithandizo cha mankhwala chaulere kuphatikizapo kuyezedwa ndi chithandizo.

Kusamala ndalama ndi chitetezo cha moyo.

- Ndalama zomwe ogwira ntchito za ulimi amalandira zikuyenera kukwezedwa poganizira ntchito yofunikira kwambiri yomwe iwo amagwira.
- Pomvana bwino, mgwirizano okhazikika wa ndalama zomwe ogwira ntchito amalandira komanso ndondomeko yake yolandirira zikuyenera kukhazikitsidwa.
- Pomwe migwirizano ngati iyi palibe, olemba anthu ntchito akuyenera kuwatsimikizira ogwira ntchito kuti adzilandira malipiro owayenera iwo ndi maanja awo kuti akhale moyo wabwino ndipo izi zikuyenera kuchitika kudzera mu zokambirana ndi bungwe lokhazikika loona za ufulu wa anthu ogwira ntchito.
- Kuika ndondomeko za kagwiridwe ka ntchito pofuna kuthana ndi kufala kwa mlirifu sikukangakhale chifukwa chochepetsera malipiro a ogwira ntchito.

- Ogwira ntchito onse kuphatikizapo oyendera nyengo, komanso omwe ndi mzika za maiko ena ndi kusatengera mmene akukhalira mdzikolo akuyenera kukhala ndi ufulu otenga tchuthi cholipidwa cha odwala kapena tchuthi chapadela, kutetezeka ku ngozi komanso chipukuta misonzi cha kulumala.



# IUF COVID-19 ZOFUNA: ZAULIMI

## Maulendo

- Ndongomeko za olemba anthu ntchito zokhudza mayend-edwe opita ndi kubwela komanso kuzungulira malo ogwira ntchito akuyenera kukhala olemkeza mpata pakati pa anthu.
- Galimoto zonyamula anthu ndi katundu zikuyenera kupopeledwa mankhwala opha tizilombo komanso ogwira ntchito akuyenera kukhala otetezedwa bwino.

## Chitetezo cha pa malo ogwira ntchito

- Malo onse ogwirirapo ntchito akuyenera kuwaika molemekeza kutalikana pakati pa anthu ndi njira zotetezera anthu kuphatikizapo zipangizo zozitetezera.
- Ogwira ntchito ma malo a ntchito akuyenera kukhala ndi mwayi okhala ndi madzi abwino, zipangizo zaukhondo komanso zovala zozitetezela ndi mankhwala opha tizilombo ndi zina.
- Uthenga okhudza komwe izi zikupezeka, komanso komwe akugawa izi ndi kugwiritsa ntchito kwake zikuyenera kupezeka kwa ogwira ntchito onse mmalo ogwira ntchito mu chiyankhulo chomwe iwo amamva.
- Kugawa komanso kugwiritsa ntchito kwa zipangizo ndi katundu kuyenera kulemekeze njira zovomelezeka zozitetezera kuphatikizapo kupopela mankhwala opha tizilombo.
- Ogwira ntchito akuyenera kuvomezedwa kuchoka pa malo a ntchito omwe iwo akuona kuti ndiosatetezeka mopanda mantha odulidwa malipiro, kuwachotsa ntchito kapena kuwatulutsa mmalo awo.
- Pakuyenera kukhala chidwi pa ufulu wa ogwira ntchito omwe ndi amayi: ufulu wawo woteteza ndalama zawo komanso chitetezo cha pa moyo wawo, kutetezeka kwa uchembele wawo, chisamaliro chawo akachira, zipangizo zozitetezera komanso chitetezo ku nkhanza zowagwiririra.

## Umoyo ndi Chitetezo

- Mgwirizano wa ogwira ntchito ndi olemba anthu ntchito oonetsetsa umoyo wabwino wa pa malo ogwira ntchito ndi makomiti oona za chitetezo ndiofunika poonetsetsa kuti njira zonse zaukhondo ndi zoteteza nzoikika bwino komanso kuti ogwira ntchito sali pa chiopsezo chiri chonse mukagwiridwe kawo ka ntchito. Amayi ogwira ntchito akuyenera kukhalapo mu ma komitiwa.

## Kuchitapo kanthu mogwirizana

- Padziko, njirazi zikuyenera kukwezedwa ndi kukhazikit-sidwa komanso kutsatiridwa ndi ogwira ntchito a boma omwe ali ndi kuthekera, olemba anthu ntchito komanso mabungwe okhazikika oona za ufulu wa anthu olembed-wa ntchito.
- Ogulitsa, kampani zokonzakudya komanso okonzakudya zinthu zakumunda akuyenera kuikapo chidwi pokhazikitsa ndondomekozi. Bungwe la United Nations' ILO, FAO ndi WHO akuyenera kuonetsetsa kuti maiko aika njira za mphamvu zoonetsetsa kuti anthu ogwira ntchito za ulimi ndi a umoyo wabwino komanso ote-tezeka. Kutsatira ofesi zawo za mdziko, akuyenera ku-kambirana ndi boma la mdzikolo ndi kuwathandiza kukhazikitsa ndondomekozi.



Mgwirizano wa bungwe loona za anthu a apa ntchito la United Nations' international Labour organization umapeleka chitsogozo chabwino cha zomwe maiko akuyenera kuchita malingana ndi ndondomeko zomwe maiko onse anagwirizana.

### Mfundo 110 – Minda ikukhudza:

- Kuteteza mafulu osankha kukhala pa bungwe ndikupeleka madandaulo mogwirizana.
- Kupeleka malipiro
- Kupeleka chithandizo cha mankhwala chabwino kwa ogwira ntchito ndi a m'banja mwawo.
- Kupeleka malo abwino okhala
- Tchuthi cholipidwa
- Kupeleka katundu ndi chithandizo mminda pa mtengo wabwino komanso ovomelezeka kuti ogwira ntchito akwanitse.
- Chitetezo kwa amayi oyembekezela, tchuthi cholipidwa cha amayi oyembekezela komanso chitetezo kwa amayi omwe angochira kumene.
- Kuyendera malo ogwira ntchito pofuna kudziwa mmene anthu akukhalira mmalo a ntchito.

### Kuti mudziwe zambiri, onani izi.

#### Mfundo 184 – Chitetezo ndi umoyo wabwino ku ulimi ikukhudza:

- Chitetezo cha umoyo ndi chitete cha ogwira ntchito za ulimi pochotsa, kuchepetsa, kapena kuunika zoopsa zomwe zingakhalepo mmalo ogwira ntchito a za ulimi.
- Kutenga nawo mbali pa ntchito yokhazikitsa komanso kuunika njira za chitetezo ndi umoyo
- Kusankha oyimirira za chitetezo ndi umoyo komanso kusankha makomiti oona za chitetezo ndi umoyo.
- Ufulu oti ogwira ntchito atha kudzychotsa okha mmalo a ntchito omwe akuoneka kuti ndioopsa ku moyo wawo.
- Ufulu oti omwe amagwira ntchito yosakhazikika ndi yoyendera nyengo adzilandira chitetezo pa umoyo ndi chisamaliro chotetezeka mmene ogwira ntchito okhazikika angalandirire.
- Kuunika chitetezo cha umoyo komanso chitetezo cha moyo poyelekeza ndi mmene ogwira ntchito mu mmagawo ena akulandirira.
- Chitetezo mmalo omwe anthu ogwira ntchito amagwiritsa ntchito makina, ndi manja, kuyendetsa, komanso kuthirira zinthu kuphatikizapo mankhwala opha tizilombo.
- Kuteteza amayi ogwira ntchito.

Kuti mudziwe zambiri, onani zothandizira izi....mfundo 192

### Kuyendera malo ogwirirapo ntchito

- Maiko akuyenera kuunika ndikukhazitsa njira zoonetsetsa kuti ndondomekozi zikutsatidwa pokhala ndi ogwira ntchito omwe ali ndi zipangizo zokwanira komanso ndiochita kalondolondo ophunzira bwino.

### Chithandizo chadzidzidzi

- Maiko akuyenera kupeleka thandizo ladzidzidzi kumadera aku midzi komwe kutseka kwa malo olova ndi kutuluka komanso misika kwaika ogwira ntchito za ulimi mmavuto komanso ntchito zawo zasokonekera. Njira zabwino zolim-bikitsira kapangidwe ka chakudya mmadela omwe anthu amakhala zikhazikitsidwe.